# CCAP GENERAL ASSEMBLY

## KALATA YOPITA KWA AKRISTU ONSE

## YOWELENGEDWA MU MIPINGO YONSE

**PA 13 JULY 2025**

## KALATA YA SINODI WAMKULU WA CCAP KUPITA KWA AKHRISTU AKE

*"INU NDINU KUWALA KWA DZIKO"*
**(MATEYU 5:14)**

**Mawu Oyamba**

Sinodi Wamkulu wa Ekelezia wa Pakati pa Afrika Chipresbeterio (CCAP General Assembly) ndi gulu la mipingo ya Chiprebeterio ya Masinodi a Livingstonia, Nkhoma, Blantyre, Zambia ndi Harare. Sinodi Waukulu ndi bwalo lalikulu kwambiri pa nkhani za ndondomeko ndi ulamulilo m'masinodiwa limene linakhazikitsidwa mu chaka cha 1924.

Chaka Chatha (2024) tinakondwerera zaka 100 za utumiki wa Sinodi Wamkulu. Mu dziko la Malawi, CCAP ndi mpingo waukulu kwambiri pa mipingo yonse ya Chiprotestanti. Mpingowu wathandiza kwambiri m'dziko muno pa nkhani zophunzitsa anthu maluso osiyanasiyana, moyo ndi chikhalidwe, ulimi ndi magawo ena ochuluka. Ambiri mwa omwe ali mu maudindo akuluakulu m'boma ndi m'mabungwe omwe si a boma mu Malawi ndi mamembala a mpingo wa CCAP. Pafupifupi zipani zonse za ndale zili ndi mamembala ambiri a mpingo wa CCAP.

Choncho, timakhulupirira kuti mamembala a CCAP ali ndi kuthekera kothandizira kusintha kwa dziko lino ngati atatsatira mokwanira mfundo za moyo wa Chikhristu m'magawo onse a moyo wawo. Komanso ali ndi kuthela kowononga dziko lino ngati satsatira mfundo za mayo wa Chikhristu.

Ife, atsogoleri a Sinodi Wamkulu wa CCAP talembela mamembala athu kalatayi ndi zolinga ziwiri: choyamba, kulimbikitsa mamembala athu kuti asakhale mbali ya mavuto omwe dziko la Malawi likukumana nawo. Chachiwiri, kuwalimbikitsa kuti akhale mbali ya njira yothetsera mavuto omwe tikukumana nawo ngati dziko. Kalatayi yagawidwa m'magawo anayi: Zokhudza Uzimu, Zokhudza Moyo ndi Chuma, Zokhudza Ulamuliro, ndi Zokhudza Ndale ndi Zisankho.

### 1. ZOKHUDZA UZIMU

Monga mpingo wokhazikika m'Mawu a Mulungu, timazindikira kuti kukula kwa moyo uzimu ndi maziko a kusintha kwa tanthauzo kwa munthu aliyense, mabanja, midzi, ndi dziko. Mfundo zotsatirazi zikulongosola malangizo athu pa zokhudza uzimu kwa mamembala onse a CCAP:

1.1. Ngakhale tikukhulupirira ndikulimbikitsa moyo wapemphero kwa Akhristu athu nonse, tikukulimbikitsaninso kuti muzigwira ntchito molimbika kuti mupeze zofunikira ndi chakudya chanu cha tsiku ndi tsiku. Tiyeni tiphunzire kwa Paulo, mmodzi wa atumwi aakulu amene anali mtumiki wa Mulungu wopemphera ndi wodzipereka, ndipo kumbali ina, iye amagwira ntchito ndi manja ake kuti apeze zofunika pa moyo wake. Mawu a Mulungu

akuchitira umboni ponena kuti "***Inu nomwe mukudziwa kuti manja angawa ananditumikira kuti tipeze zimene ine ndi anzanga tinkazifuna"*** (Machitidwe 20:34).

1.2. Tikulimbikitsa mamembala onse a CCAP kuti akhale kuwala mu dziko lathu, nthawi zonse, kulikonse komanso muzochitika zilizonse. Mawu a Mulungu akuti ***"Momwemonso, muwalitse inu kuunika kwanu pamaso pa ena, kuti pakuona ntchito zanu zabwino, alemekeze Atate wanu wa Kumwamba"*** (Mateyu 6:16).

1.3. Tikuchenjeza mamembala onse a CCAP kuti asatsate ziphunzitso zonyenga ndi mauneneri abodza. Kumbukirani zimene Yesu Kristu ananena kuti ***"Ndipo aneneri onyenga ambiri adzauka, nadzasokeretsa ambiri"*** (Mateyu 24:11). Komanso Mawu a Mulungu kudutsira mwa mtumwi Petro kuti ***"M'chisiriro chawo aphunzitsi awa adzakudyerani masuku pamutu ndi nthano zopeka"*** (2 Petro 2:3).

1.4. Tikulimbikitsa mamembala onse a CCAP kuti kupatula kulalikila za chikondi ndi umodzi, chofunika kwambirir ndi kuti akhale mu zimenezi. Ngakhale timachokera ku zigawo zosiyana, maboma osiyana, ndi mitundu yosiyana, ndife amodzi mwa Khristu ndipo tili ndi udindo woperekedwa ndi Mulungu wogwirizanitsa dziko lathu. Ngakhale Yesu adatipempherera kuti tikhale amodzi (Yohane 17:11)

1.5. Ngakhale tikuvomereza kufunika kwa intaneti ndi malo ochezera a pa Intaneti, tikulimbikitsa mamembala onse a CCAP kuti apitilize kusonkhana ndi ena, m'malo mozolowela chikhalidwe chopembedza pogwiritsa ntchito malo ochezera a pa Intaneti. Mawu a Mulungu amatilimbikitsa kuti ***"Tisaleke kusonkhana kwathu pamodzi, monga achitira ena, koma tilimbikitsane, makamaka tsopano, popeza tsiku la kubweranso kwake likuyandikira"*** (Ahebri 10:25).

1.6. Tikulimbikitsanso mamembala onse a CCAP omwe ali m'mudindo m'boma ndi mabungwe omwe siaboma kuti agwiritse ntchito mwayi wawo kulimbikitsa makhalidwe olemekeza Mulungu. Tikupempha makamaka amene ali m'nthambi zitatu za boma; Nthambi Yoyendetsa Boma (Executive), Nthambi Yoweluza Milandu (Judiciary) ndi Nthambi Yopanga Malamulo (Legislature) kukhala zitsanzo zabwino. Chifukwa cha kupezeka kwanu m'maudindo amenewo, Amalawi akuyenera kusangalala osati kubuula chifukwa cha khalidwe lanu. Mawu a Mulungu akutsimikiza kuti ***"Anthu olungama akamalamulira m'dziko anthu amakondwa, koma ngati dziko lilamulidwa ndi anthu oyipa mtima anthu amadandaula"*** (Miyambo 29:2)

## 2. ZOKHUDZA MOYO NDI CHUMA

Poganizira za mavuto omwe tikukumana nawo pa chikhalidwe cha anthu ndi zachuma, ndikofunika kuvomereza zimene zikuyenda bwino komanso ntchito yomwe yatsala. Mfundo zotsatirazi zikuwonetsa zina mwa zinthuzi

ndikudandaulila mamembala a CCAP kuti achitepo kanthu pofuna kukonza zinthu.

2.1. Pamene tinali ndi chikondwerero cha kuti CCAP yakwanitsa zaka 100 chaka chatha (2024), tinabweretsa poyera zomwe tathandizira polimbana ndi adani atatu omwe ife, monga dziko tinazizindikira m'chaka chomwe tinalandira ufulu wodzilamulira: njala, nthenda ndi nsanje. Adani atatuwa anakhala mbali ya nyimbo yathu ya fuko kuyambira mu 1964. Koma n'zomvetsa chisoni kuti awa akadali adani a Malawi mpaka pano. Tikupempha mamembala onse a CCAP ndi mabungwe ena achikhristu kuti adzuke ndikukhala odzetsa kusintha. Tisadalire andale kuti athetse njala, kaduka ndi matenda.

2.2. Tikuyamikira Boma chifukwa cha zinthu zabwino zomwe zathandiza Amalawi monga kagawidwe ka chakudya kwa anthu ovutika m'madera osiyanasiyana m'dziko muno, kumangidwa kwa misewu yabwino m'madera osiyanasiyana m'dziko muno, kugawidwa kwa ngongole za NEEF ndi kupereka ndalama kwa anthu osawuka, ndi zina zambiri. Tikupempha mamembala onse a CCAP omwe ali mbali ya utsogoleri m'madipatimenti ndi mabungwe awa kuti agwire ntchito mwachilungamo. Ngati Sinodi Wamkulu wa CCAP:

a) Sitikuyembekezera ntchito zosalongosoka pomwe mamembala a CCAP ali gawo la akuluakulu oyang'anira ntchitozi
b) Sitikuyembekezera katangale ndi kuba komwe mamembala a CCAP ali mbali ya utsogoleri
c) Sitikuyembekezera tsankho ndi kukondera kumene mamembala a CCAP akutenga nawo mbali potsogolera ndondomeko ya zisankho
d) Sitikuyembekezera kukanidwa kapena kuchedwa kwa chilungamo pomwe mamembala a CCAP ali mbali ya utsogoleri

2.3. Kugulitsa katundu amene masiku ake ogwira ntchito adatha ndi amalonda ena. Tawona ndi nkhawa yayikulu kuti amalonda ena akugulitsa zinthu zomwe masiku ake ogwiritsa ntchito adatha. Sizobisa kuti amalonda ena apezeka akuchotsa masiku otha mphamvu katundu ndikuyika masiku atsopano. Khalidweli ndi loipa ndipo siziyenera kuloledwa m'Malawi muno. Tsoka ilo, amalondawa akugwiritsa ntchito a Malawi kuchita zoipazi. Tikupempha mamembala onse a CCAP ndi a Malawi onse akufuna kwabwino kuti aziulura mchitidwe woipawu ku mabungwe a boma omwe amawona za malonda

2.4. Zotsatira za Kusintha kwa nyengo zikubweretsa zovuta zambiri zomwe tikukumana nazo padziko lonse lapansi komanso ngati dziko la Malawi. Masiku ano, chilala ndi mphepo zamkuntho zasokoneza dziko la Malawi. Komabe, zina mwa zotsatira za kusintha kwa nyengo zomwe tikukumana nazo ndi zopangidwa ndi anthu. Ngati utsogoleri wa Sinodi Wamkulu wa CCAP:

a) Tikulimbikitsa mamembala onse a CCAP kuti asadule mitengo yotsala. M'malo mwake ayenera kutenga nawo mbali kubzala mitengo kapena kuteteza zitsamba kuti zikule.
b) Tikulimbikitsa mamembala onse a CCAP kuti asamange nyumba m'mphepete mwa mitsinje ndi madambo, m'malo mwake agwiritse ntchito mitsinje kulima mbewu. Utsogoleri wa CCAP ukulimbikitsanso mamembala onse a CCAP kuti asamange nyumba ndi kulima m'mphepete mwa mapiri kuti apewe kutaya katundu ndi miyoyo pa nthawi ya kugumuka kwa mapiri.
c) Tikupemphanso mamembala athu kuti asagulitse zinthu zochepa zomwe akolola chaka chino.
d) Tikuletsa mamembala onse a CCAP kuti asagulitse malo awo. Simungathe kuthetsa umphawi pogulitsa katundu monga malo
e) Tikulimbikitsa mamembala onse a CCAP kuti asadalire boma ndi andale kuti ndiwo athetse umphawi ndi njala yathu.
f) Tikulimbikitsa andale onse a CCAP omwe ali m'boma ndi azipani zotsutsa kuti asagwiritse ntchito umphawi ndi njala ngati zida za kampeni.

2.5. Utsogoleri wa Sinodi Wamkulu wa CCAP ukukumbutsa mamembala onse a CCAP kuti tigwirane manja pothetsa maukwati a ana, ndi khalidwe lililonse lozunza ana. Abusa onse a CCAP akukumbutsidwa kuti asamamange maukwati a anthu ochepera zaka 18. Makolo akukumbutsidwa za udindo wawo wopatsidwa ndi Mulungu wokonda ndi kusamalira ana awo. Musalole kapena kukakamiza ana anu kukwatiwa asanakwanitse zaka 18.

2.6. Nkhanza kwa Amuna ndi Akazi zilibe malo m'nyumba za mamembala onse a CCAP. Kuzunza munthu potengela chibadwidwe chake kuti ndi mkazi kapena mwamuna ndi khalidwe loipa. Chonde nenani kwa atsogoleri a mpingo wanu komanso ku polisi ngati mukukumana ndi zotere.

2.7. Mamembala onse a CCAP akupemphedwa kuti asamaononge nthawi yawo pa masamba a mchezo. Tiyeni tigwiritse ntchito nthawi mwanzeru komanso mwaphindu. Komanso, musagwiritse ntchito malo ochezera a pa Intaneti kuti mufalitse miseche ndi kuwononga mbiri ya ena monga Mawu a Mulungu akuchenjeza kuti ***"Musamanene zabodza, ndipo musathandize wolakwa popereka umboni wonama, musatsatire ochuluka pamene achita zoipa, kapena popereka umboni wopotoza chilungamo"*** (Eksodo 23:1-2)

### 3. ZOKHUDZA ULAMULIRO

Ulamuliro wabwino ndiwo maziko a mtendere, bata, ndi chitukuko cha dziko. Akhristu tidaitanidwa kuti tizisunga ndi kulimbikitsa kuchita zinthu mwachilungamo ndi kugwira ntchito moyenera mu nthambi zonse zikuluzikulu monga zachitetezo

ndi makhothi, omwe ndi ofunikira kwambiri pakuwonetsetsa chilungamo ndi bata m'dziko. Mfundo zotsatirazi zikufotokoza zimene ife tikuona pa nkhani za ulamuliro.

3.1. **Chitetezo:** Nthambi za achitetezo zidakhazikitsidwa kuti zizitumikira Amalawi mwachilungamo. Mwatsoka, anthu ena omwe amagwira ntchito mu nthambi zachitetezo sakugwira ntchito mwaukadaulo monga momwe Amalawi amayembekezera. Tikulimbikitsa mamembala onse a CCAP omwe amagwira ntchito nthambi zosiyanasiyana zachitetezo kuti agwire ntchito yawo mwaukadaulo, ndikumakumbukira kuti pamapeto pake adzayankha mlandu kwa Mulungu. Amene ali m'maudindo a ulamuliro sayenera kugwiritsa ntchito nthambi zachitetezo kufooketsa ndi kupondereza ena. Amalawi onse akuyenera kutumikiridwa mofanana komanso mwachilungamo.

3.2. **Nthambi ya Chiweruzo:** Ngakhale tikuthokoza Pulezidenti wa Dziko chifukwa choonjezera chiwerengero cha anthu ogwira ntchito m'mabwalo amilandu, pali kuchedwa poyendetsa milandu yomwe ikufunika chilungamo mwamsanga. Posachedwapa pakhala milandu yakatangale m'mabwalo amilandu, chinthu chomwe ndi chodetsa nkhawa. Tikupempha mamembala onse a CCAP omwe ali m'mabwalo amilandu kuti akane ziphuphu zamtundu uliwonse. Mawu a Mulungu akuchenjeza kuti **"Usalandire chiphuphu, pakuti chiphuphu chimachititsa khungu iwo amene akuona ndi kupotoza mawu a wosalakwa."** (Eksodo 23:8) ndi kutinso, **"Musamakhotetse chiweruzo kapena kukondera. Musamalandire chiphuphu pakuti chiphuphu chimadetsa m'maso anthu a nzeru ndi kusintha mawu awo kuti mlandu uyipire osalakwa** (Deuteronomo 16:19).

3.3. **Katangale:** Pamene ulamuliro umene ulipo unkalowa m'boma, panali lonjezo lothetsa katangale m'Malawi. Sizobisa kuti katangale akupitilira kukula m'dziko lathu. Sinodi Wamkulu akunenetsa kuti:

a) Katangale akuchitika pai kugulitsa ndi kugula katundu, m'maofesi, pakati pa atsogoleri a magulu onse.

b) Ndife okhumudwa kuti mamembala ena a CCAP akutenga nawo mbali muzakatangale kudzera m'malo awo antchito ndi malo abizinesi.

c) Tikupempha mamembala onse a CCAP omwe akugwira ntchito m'ma ofesi osiyanasiyana, ochita mabizinesi osiyanasiyana, okhala ndi maudindo osiyanasiyana kuti asiye katangale wamtundu uliwonse.

3.4. **Kuchita Zinthu Poyera ndi Kutenga Udindo Woyankha.** Kuchita zinthu poyera ndi kulumikizana momasuka komanso moona mtima, pomwe kutenga udindo ndi kuvomera zotsatira za zimene tikuchita. Tsoka ilo, zikuwoneka kuti pali kuchita zinthu poyera ndi kutenga udindo pa zinthu

pang'ono kapena ayi pa omwe ali pamaudindo a utsogoleri masiku ano. Mawu athu ndi akuti:

a) Payenera kukhala khalidwe lochita zinthu poyera ndi kutenga udindo pa zimene tikuchita pakati pa anthu onse mu utsogoleri pa momwe amagwiritsira ntchito ndalama za msonkho komanso za Mulungu.
b) Amalawi ali ndi chidwi chofuna kudziwa momwe ndalama za boma zikugwiritsidwira ntchito. Mwachitsanzo, pali kubisa kwambiri za mmene ndalama zotukulira madera a aphungu a nyumba ya malamulo (CDF) zikuyendetsedwera.
c) Tikupempha aphungu a nyumba yamalamulo ndi anthu onse omwe ndi a CCAP komanso omwe akukhudzidwa ndi kagwiritsidwe ntchito ka ndalama za boma kuti akhale anthu achilungamo. Kumbukirani kuti choyamba timayankha kwa Mulungu tisanayankhe kwa anthu.
d) Mu mzimu womwewo, tikukumbutsanso atsogoleri a mipingo ndi madipatimenti onse a CCAP kuti kuchita zinthu mowonekera ndi kukhala ndi udindo woyankha kuyenera kutsatiridwa ndi mtima onse.

3.5. **Ndalama Zakunja**: Sizobisa kuti chuma cha Malawi chasokonekera chifukwa cha kusowa kwa ndalama zakunja. Izi zapangitsa kukwera kwa mitengo ya chilichonse komanso kusowa kwa zinthu zina zofunika. A Malawi akudutsa mu nyengo zowawa ndithu. Ngakhale tikudziwa kuti padziko lonse pali mavuto a zachuma, pali zinthu zina zomwe ziyenera kuthetsedwa momwe boma lathu limayendetsera chuma chake. Boma likuyenera kupeza njira zowonjezerera ndalama zakunja m'dziko muno. Tikukulimbikitsani mamembala onse a CCAP kuti apewe kuchita malonda osaloledwa a ndalama zakunja.

3.6. **Migodi**: Miyala yamtengo wapatali yapezeka pafupifupi m'Malawi yense. Izi zasinthadi chuma cha Malawi. Komabe, nkhawa ya utsogoleri wa Sinodi Yaikulu ya CCAP ndi kuchuluka kwa katangale zomwe zakula kwambiri m'Malawi. Ngati Sinodi Wamkulu wa CCAP tikuti:

a) Kuchedwa kuyamba kukumba migodi kukudetsa nkhawa kwambiri chifukwa pali anthu omwe akuchita malonda a miyalayi ndipo boma likudziwa. Tidauzidwa ndithu kuti Banki Yaikulu m'Malawi ikugula miyala imeneyo. Sitikudziwa ngati akugula yonse kapena ina mwa miyalayi.
b) Nkhani yotenga miyala yokayezedwa ikupitilira. Tamva kuti miyala yathu ndi yapamwamba kwambiri komanso yochuluka kwambiri komabe pali kusuntha pang'ono kapenaso palibe chimene chikuchitika kuti tiyambe kuchita ntchito za migodi.
c) Ndi chipongwe kuti dziko la Malawi likhale ndi 10% ya phindu lomwe limachokera ku malonda a miyala monga momwe mphekesela zikumvekela. Dziko la Malawi siliyenera kulamulidwa ndi kuchedwetsedwa ndi ndondomeko za mayiko akunja. Boma ndi

okhudzidwa onse agwire ntchito mwachangu kuti atsitsimutse chuma chathu chomwe chikufa.

d) Tikupempha mamembala onse a CCAP omwe akukhudzidwa ndi gawo la migodi kuti akhale m'gulu la osintha zinthu, ndipo asagwirizane ndi omwe angafune kuchedwetsa kapena kubweretsa katangale ndi ndale mu ntchito za migodizi.

## 4. ZOKHUDZA NDALE NDI CHISANKHO

Mpingo uli ndi udindo wotsogolera okhulupilira momwe angakhalire ngakhale pa nkhani za ndale maka pamene tikuyandikira ku chisankho. Utsogoleri wa Sinodi Wamkulu wa CCAP ukutsindika mfundo zotsatirazi pofuna kuteteza ungwiro wa Mpingo ndi kulimbikitsa kutengapo mbali mwamtendere.

4.1. Tisalole kugwiritsidwa ntchito ndi andale. CCAP ndi mpingo osati chipani cha ndale.

4.2. Osagwiritsa ntchito amene akupikisana pa mipando ya ndale ngati njira yopezera ndalama za mpingo. Pali chizolowêzi choitana andale amene akupikisana pa maudindo ku mipereko yapadera ya mpingo kuti apikisane pakaperekedwe ka ndalama. Mchitidwewu sukuyenera kupitirira. Tisapange mpingo wa Mulungu kuoneka wozingwa ndi wosowa pogwira. Tiyeni tigwiritse ntchito njira za m'Baibulo zopezera ndalama ndi zothandizira mpingo.

4.3. Utsogoleri wa Sinodi Wamkulu wa CCAP ukukumbutsa abusa ndi onse amene amakwela pagome kuti asagwiritse ntchito gome kulalikila ndale koma Mawu a Mulungu. Atumiki tonse tinaitanidwa ndi Mulungu, ndipo tidzayankha mlandu kwa Mulungu. Choncho, tiyenera kuopa ndi kukondweretsa Mulungu yekha.

4.4. Ngakhale tikuvomereza kuti aliyense ali ndi ufulu wotsatira chipani cha ndale chomwe akufuna, musagwiritse ntchito mpingo wa CCAP kupititsa patsogolo zolinga za ndale.

4.5. Utsogoleri wa Sinodi Wamkulu wa CCAP ukudzudzula ziwawa zamtundu uli wonse zomwe zikuchitika m'dziko lathu. Tikupempha mamembala onse a CCAP kuti asatenge nawo mbali pa ziwawa zonse zakudza chifukwa cha ndale. Tikulimbikitsanso mamembala onse a CCAP omwe ali ndi maudindo m'nthambi za chitetezo za boma kuti agwiritse ntchito mphamvu zawo kuletsa ziwawa zamtundu uliwonse, komanso kumanga omwe akuyambitsa ziwawa. Tikuyembekeza kuti mamembala onse a CCAP awonetsera za khalidwe la Chikhristu monga ana a Mulungu m'magawo zonse a moyo wawo. Mawu a Mulungu amatiphunzitsa kuti "Odala ali akuchita mtendere, chifukwa adzatchedwa ana a Mulungu" (Mateyu 5:9). Choncho, tikutsutsa ziwawa zamtundu uliwonse m'dziko lathu.

4.6. Onse okhudzidwa ndi kutenga nawo mbali pakukonzekera ndi kuyendetsa zisankho akuyenera kuwonetsa chilungamo kwa onse. Pakufunika kuchita zinthu poyera ndi mwachilungamo m'njira zonse zoyendetsera zisankho. Tikupempha mamembala onse a CCAP omwe ali mu bungwe loyendetsa

zisankho la Malawi Electoral Commission ndi mabungwe ena omwe akukhudzidwa ndi kayendetsedwe ka zisankho zomwe zikubwera, kuti azigwira ntchito yawo mokhulupirika podziwa kuti poyamba penipeni adzayankha kwa Mulungu.

4.7. Posachedwapa, pakhala madandaulo chifukwa cha mchitidwe wachinyengo m'zipani zosiyanasiyana za ndale momwe achitira misonkhano yawo yayikulu yosankha atsogoleri ndi zisankho zamapulaimale. Ndizomvetsa chisoni kuti ena mwa anthu omwe akutsogolera mchitidwewu ndi Akhristu, ndipo ena ndi mamembala a CCAP. Atsogoleri a CCAP akudzudzula khalidweli. Lolani anthu kuti asankhe atsogoleri omwe akufuna.

4.8. Utsogoleri wa Sinodi Wamkulu wa CCAP ukutsatira mwachidwi zokambirana za migwilizano ya zipani za ndale yomwe ingachitike pokonzekera zisankho zomwe zikubwerazi. Langizo lathu ndi lakuti zipani za ndale zipange mgwirizano mwachilungamo. Amalawi sali okonzeka kutsogozedwa ndi migwirizano yopangidwa ndi zipani za ndale zomwe utsogoleri wawo ndi wadyera. Mgwirizano uyenera kubweretsa pamodzi atsogoleri omwe ali ndi mbiri yabwino komanso okonda Amalawi osati mtundu, dera kapena chipembedzo chawo. Tikulimbikitsa mamembala onse a CCAP kuzipani zosiyanasiyana kuti achitepo kanthu kuti zipani zawo ziziyenda bwino. Tiyeni titsate mawu amene Yesu anatilangiza kunena kuti, **"Inu ndinu kuwunika kwa dziko lapansi. Mzinda womangidwa pa phiri sungathe kubisika. Anthu sayatsa nyale ndikuyivundikira ndi mbiya, m'malo mwake amayika poonekera ndipo imawunikira onse m'nyumbamo. Momwemonso kuwunika kwanu kuwale pamaso pa anthu kuti aone ntchito zanu zabwino ndi kulemekeza Atate anu akumwamba"** (Mat. 5:14-16)

4.9. Utsogoleri wa Sinodi Wamkulu wa CCAP ukulimbikitsa onse amene adalembetsa kuti apite kukaponya mavoti awo. Tiyeni tisavote motengera mtundu, dera kapena chipembedzo. Tiyenera kuvotela utsogoleri umene masomphenya ake adzatukula dziko kuti aliyense apindule. Mawu a Mulungu akutilangiza kuti **"Koma sankha amuna odziwa ntchito yawo, anthu owopa Mulungu, anthu odalirika amene amadana ndi kupeza phindu mwachinyengo"** (Eksodo 18:21)

4.10. Pamene tikupita kukavota, tiyeni tiganizire za atsogoleri omwe ali ndi chidwi chokweza chuma cha dziko lathu. Tiyeni tiganizire za anthu amene adzakhaladi ndi mtima wofunitsitsa kukwaniritsa malonjezo awo. Tisavotere atsogoleri omwe sangathe kukwaniritsa malonjezo awo komanso sangakhale okonzeka kuyankha pa zimene akuchita.

4.11. Mamembala onse a CCAP tikuwalangiza kwambiri kuti asavotere atsogoleri ndi zipani za ndale zomwe zimagwiritsa ntchito ziwawa potsekereza ndi kupondereza ena.

**MAWU OMALIZA**

Utsogoleri wa Sinodi Wamkulu wa CCAP ukupempha mamembala onse kukhala ogwirizana, kukondana wina ndi mzake, komanso kusamalirana. Tiyeni tipempherere dziko lathu m'nyumba zathu ndi m'mipingo yathu. Kumbukirani zimene Yehova anauza Aisrayeli kudzera mwa Yeremiya kuti: **"Ndiponso muzifunafuna mtendere ndi ubwino wa mzinda umene ndinakupirikitsirani ku ukapoloko. Muzipempherera mzindawo kwa Yehova, kuti zikuyendereni bwino"** (Yeremiya 29:7).

**Mulungu akudalitseni. Mulungu adalitse Malawi!**

**Ife atsogoleri anu:**

Rt. Rev. Biswick Kamzongo Nkhoma
**MTSOGOLERI WA SINODI WAMKULU WA CCAP**

Rev. Dr. Mwai Chilongozi
**MLEMBI WAMKULU WA SINODI WAMKULU**

Rev Edward Masona Tembo Kaluluma
**MTSOGOLERI, NKHOMA SINODI**

Rev. Vasco Kachipapa
**MLEMBI WA ZONSE, NKHOMA SINODI**

Rev. Dr. Hamphreys Zyambo
**MTSOGOLERI, BLANTYRE SINODI**

Rev. Anderson Juma
**MLEMBI WA ZONSE, BLANTYRE SINODI**

Rev. Jairos Kamisa
**MTSOGOLERI, LIVINGSTONIA SINODI**

Rev. William Tembo
**MLEMBI WA ZONSE, LIVINGSTONIA SINODI**